

Banja laling'ono, umoyo wathanzi mboma la Dedza

Banja la anthu ochepa limapindula mokwanila kuchokela ku zithandizo zosiyanasiyana za mdziko zokhudza miyoyo yawo

- Mu zaka makumi awiri zapitazi chiwerengero cha anthu mboma la Dedza chaonjezeleka ndi theka kuchoka pa anthu 114 kufika pa anthu 172 pa km² ili yonse.
- Nyumba zokhala anthu ziwiri (2) mwa nyumba zitatu (3) zili zonse zili ndi potunga madzi a ukhondo pa makono.



Nyumba zokhala anthu zisanu ndi zinayi (9) mwa nyumba khumi (10) zili zonse zimagwiliitsa ntchito nkhuhi pophika; ndipo nyumba imodzi (1) yokha mwa nyumba makumi khumi (100) zili ndi magetsi.




Amayi amodzi (1) okha mwa amayi makumi khumi (100) aliwonse; komanso abambo awiri (2) okha mwa azibambo makumi khumi (100) aliwonse ndi amene amamaliza maphunziro awo a ku sekondale.

- Amayi amodzi (1) okha mwa amayi awiri (2) aliwonse komanso abambo atatu (3) mwa abambo anayi (4) aliwonse amadziwa kulemba, kuwelenga ndi kuwelengera.
- Amayi makumi awiri ndi mphambu ziwiri (22) mwa amayi makumi khumi (100) aliwonse komanso abambo asanu ndi atatu (8) mwa abambo makumi khumi (100) aliwonse sali pa ntchito iliyonse yolembedwa.
- Amayi atatu (3) mwa amayi asanu (5) aliwonse amavutika kwambiri kupeza chithandizo cha mankhwala akadwala chifukwa zipatala zoyandikila ndi kumene amakhala zili kutali kwambiri.

Ubwino wotsatira njira za kulera

Banja likakhala ndi ana ochepa, zimathandiza makolo a anawa kuwaphunzitsa mokwanila ana awo ndipo chifukwa choti aphunzira bwino, anawa amakhala ndi mwayi wojeza ntchito zabwino mtsogolo. Kuchepetsa kachulukidwe ka anthu mdziko kumathandiza boma ndi mabungwe othandiza boma kukonzekera bwino pa ntchito zopititsa umoyo wa anthu patsogolo monga kukhala ndi madzi a ukhondo, ntchito za umoyo komanso za mtengatenga.

Anthu awiri mwa anthu atatu aliwonse mbomali ali ndi zaka zosapitilira makumi awiri ndi zisanu (25)



Source: National Statistical Office of Malawi, Population Projections Malawi.

Banja la anthu ochepa limakhala ndi mayi wa moyo wathanzi komanso banjalo limakhala losangalala



Amayi amabeleka ana asanu (5) kapena asanu ndi mmodzi (6) pa moyo wao wonse koma amaonetsa chidwi chobeleka ana atatu (3) kapena anayi (4) wokha pa moyo wao wonse.



Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu (5) aliwonse a zaka za pakati pa khumi ndi zisanu (15) ndi zaka khumi ndi zisanu ndi zinayi (19) ayamba kale kubeleka ana.

- Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu (5) aliwonse amabelekela kunyumba osati kuchipatala.
- Amayi atatu (3) mwa amayi asanu ndi awiri (7) aliwonse omwe ali pa banja amatsata njira za kulera; ndipo amayi amodzi (1) mwa amayi atatu (3) aliwonse amatsatira njira zolererazi kuti asabeleke ana ambiri.
- Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu ndi amodzi (6) aliwonse komanso abambo amodzi (1) mwa abambo asanu (5) aliwonse amakhulupilira kuti ndi zovomelezeka kuti mamuna akhoza kumenya mkazi wake nthawi zina.

Ubwino wotsatira njira za kulera


Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu ndi amodzi (6) aliwonse a zaka zapakati pa khumi ndi zisanu (15) ndi makumi anayi ndi zisanu ndi zinayi (49) amamwalira pa nthawi yobeleka mwana. Kutsatila njira za kulera kumathandiza amayi omwe ndi achichepeleko kutenga nthawi asanakhale ndi mimba (pathupi) ndipo kutenga nthawi chonchi kumathandiza kuti asapeze mavuto nthawi mwawo omwe amadza chifukwa chobeleka akadali ang'ono. Amayi ngati akhala ndi ufulu wosankha nthawi yoti abeleke komanso kusiyantsa zaka za ana obelekedwa zimawathandiza kuti akhale ndi moyo wathanzi. Ana omwe amayi awo anamwalira nthawi zambiri samamaliza maphunziro awo ku sukulu.

Mdziko la Malawi, amayi amodzi amamwalira pobeleka ana pa ma ola awiri aliwonse.

Mwana wakhanda mmodzi wosakwana chaka chimodzi amamwalira ma ola asanu aliwonse.

Banja la anthu ochepa ana ake amakula bwino komanso amakhala ndi moyo wathanzi

- Mwana mmodzi (1) mwa ana asanu ndi mmodzi (6) aliwonse wochepera zaka zisanu (5) amakhala ndi thupi lopelewela losagwilizana ndi msinkhu wawo.



Mwana mmodzi (1) mwa ana awiri (2) aliwonse wochepera zaka zisanu (5) amakhala wopinimbira.

Ubwino wotsatira njira za kulera

Kutsatila njira za kulera kumathandiza ma banja kuti ana awo akule ndi moyo wathanzi komanso kutha kuonetsetsa kuti pakupita nthawi yokwanila bwino pamene mwana wabadwa ndi nthawi yomwe mwana wina akudzabadwanso mbanjamo. Ana obadwa mosiyana ndi zaka zitatu kapena kupitilira apo amakhala ndi mwayi wokhala moyo wochulukira kwambiri kuposa ana omwe abadwa mosiyana ndi zaka ziwiri kapena kuchepela apo. Makolo omwe ali ndi ana ochepa amasalira bwino ana awo ndi kuwapatsa zakudya zokwanila.

Pa ma ola awiri aliwonse mwana mmodzi wosakwanitsa zaka zisanu amamwalira.